Phunziro 13, June 29, 2024




# KUGONJETSA KWA CHIKONDI CHA MULUNGU

"Ndipo ndinamva mau akulu ochokera ku mpando wachifumu, ndi kunena Taonani, chihema cha Mulungu chili mwa anthu; ndipo adzakhalitsa nao, ndi iwo adzakhala anthu ake, ndi Mulungu yekha adzakhala nao, Mulungu wao; 4ndipo adzawapukutira misozi yonse kuichotsa pamaso pao; ndipo sipadzakhalanso imfa; ndipo sipadzakhalanso maliro, kapena kulira, kapena chowawitsa; zoyambazo zapita"

(Chivumbulutso 21:3, 4)





Mkangano waukulu, umene Satana anapandukira boma la Mulungu, ukufika kumapeto mofulumira.

Sitinasiyidwe mumdima pa zam'mene mkanganowu uti udzathere: Mulungu adzapambana, Satana adzalephera.

Ngakhalenso tsatanetsatane wa nkhondo zomalizira wafotokozedwa momveka bwino mu Baibulo.





- Nthawi ya zowawa ndi kumasulidwa.
- Nthawi ya mantha akulu ndi chisangalalo.
- Nthawi ya chiwonongeko ndi chiweruzo.
- Nthawi ya moyo ndi imfa.
- Nthawi yokonda ndi kukondedwa.

# NTHAWI YA ZOWAWA NDI KUMASULIDWA

"Kalanga ine! Pakuti nlalikulu tsikulo, palibe lina lotere; ndi nthawi ya msauko wa Yakobo; koma adzapulumuka m'menemo" (Jeremiya 30:7)

"Tikukhala mu nyengo yakumapeto. Zizindikilo zokwanilitsa za kuti kudza kwa Khristu kuli pafupi zikuonekera mwa msanga. Masiku amene tikukhala ano ndi ofunikira kwambiri." (EGW, TI9, 11) . Kodi zochitikazi zidzakhala zotani?

**Chiv. 22:11**



Chiweruziro chatha ndipo mulandu uliwonse wagamulidwa. Khomo la chisomo latsekedwa.

**Yes. 8:21-22; Yer. 30:7**



Nthawi ya zowawa. Oipa akuchita zinthu mosadziletsa, Ndipo olungama sakudziwa ngati akhululukidwa.

**Chiv. 15:7-8; Mal. 27:5**



Miliri 7 yomaliza ikugwera anthu osalapa. Anthu a Mulungu akulonderedwa ndi kutetezedwa.

**Chiv. 16:14; 1Yoh. 3:2-3**



Gulu lirilonse likonzekera kukumana ndi Yesu. Ena kuti amenyane naye; enawo kuti amulandire mwa chisangalalo.


Pamene Yesu adzamalize ntchito yake yopembedzera ndipo Mzimu Woyera adzachoka kwa anthu osalapa, tsogolo la munthu aliyense lidzakhala litasindikizidwa. Okhulupirika adzapitirizabe kulandira chithandizo ndi chitetezo kuchokera kwa Mulungu, pamene oipa adzakhala akuzunzidwa ndi Satana. Aliyense adzaonetsera chikhalidwe cha yemwe anasankha kumtumikira.

# NTHAWI YA MANTHA AKULU NDI CHISANGALALO

"Nanena kwa mapiri ndi matanthwe, Igwani pa ife, ndipo tibiseni ife kunkhope ya Iye amene akhala pa mpando wachifumu, ndi kumkwiyo wa Mwanawankhosa" (Chivumbulutso 6:16)

Iwo akana Chilamulo cha Mulungu; Iwo akana madzi amoyo ndipo adzikumbira okha "zitsime zong'aluka" (Yeremiya 2:13).

Tsopano iwo akuyang'anizana maso ndi maso ndi Woweruza. Chomwe angayembekezere ndi mkwiyo ndi kutsutsidwa kokha. Kodi amene adzawamasule ndi ndani? (Yesa. 2:19; Chiv. 6:16).



"Ndipo adzanena tsiku limenelo, Taonani, uyu ndiye Mulungu wathu; tamlindirira Iye, adzatipulumutsa; uyu ndiye Yehova, tamlindirira Iye, tidzakondwa ndi kusekerera m'chipulumutso chake" (Yesaya 25:9)



Iwo akhala okhulupirika ku Malamulo a Mulungu; Iwo amwa madzi a moyo (Chibvumbulutso 21:6). Tsopano akuyang'anizana maso ndi maso ndi Woweruza wawo. Chomwe angayembekezere ndi chipulumutso chokha. Kodi ndi chiyani chingawakanikitse kutsanula matamando? (Yesaya 25:9; Chivumbulutso 15:3-4).

- Satana akwiyira otsala (Chiv. 12:17)
  - Amapangitsa aliyense kuti amulambire ndi kumvera malamulo ake (Chiv. 13:15-17) → Akukonzetsera dziko lapansi kuti limenyane ndi Mwanawankhosa (Chiv. 17:12-14) → Yesu akuwononga adani ake onse pa Kubwera kwake (Chiv. 19:11-15)
  - Otsala akhalabe okhulupirika ku Malamulo a Mulungu (Chiv. 14:12) → Amakonzekera kukumana ndi Mulungu wake (Amosi 4:12) → Yesu akutenga kwa Iye mwini onse omwe anakhulupilira mwa Iye (Chiv. 19:6-8)

# NTHAWI YA CHIWONONGEKO

"Dziko lidzapulululuka konse, ndi kupasulidwa ndithu; pakuti Yehova anenana mau amenewa." (Yesya 24:3)




**Pamene Yesu akubwera, oyera omwe anakhala mibadwo yonse adzaukitsidwa; ndipo pamodzi ndi omwe adzakhale ali moyo koma okhulupirika, atasanthulidwa, adzapita nawo limodzi Kumwamba ndi Yesu (1 Atesalonika 4:16-17).**

**Anthu oipa adzafa pamaso pa Yesu. Mitembo yawo idzakhala yosakwiriridwa, ndipo potsirizira pake, sipadzalanso moyo womwe udzatsalira pa Dziko Lapansi (Yeremiya 25:33; Chivumbulutso 19:17-21; Yeremiya 4:23-26; Yesaya 24:3).**



**Pa nthawiyo, Satana ndi angelo ake adzatsekeredwa ku phompho kwa zaka zana limodzi, osathanso kunyenga aliyense (Chivumbulutso 20:1-3).**

**Mawu oti Phompho, (malo a m'dima), akufotokozera momveka bwino za m'mene dziko lapansi liti lidzaonekere/kusandulikira pa nthawiyo. Popanda munthu wa moyo pa dziko lapansi, yemwe chiwanda chilichonse chidzayese. Idzakhala nthawi yoti angelo opanduka athe kusinkhasinkha za kupanduka kwawo, ali omangidwa ndi unyolo wa zochitika, ali popanda mwayi wochoka pa Dziko Lapansi labwinja.**



# NTHAWI MAYESERO

"Ndipo ndinaona mipando yachifumu, ndipo anakhala pamenepo; ndipo anawapatsa chiweruziro; […] ndipo anakhala ndi moyo, nachita ufumu pamodzi ndi Khristu zaka chikwi" (Chivumbulutso 20:4)



Ngati Chiweruzo chinakondwerereedwa kudzanso kwachiwiri kusanachitike, ndipo Yesu adapereka kale chiweruzo, kupereka moyo wosatha kwa iwo amene adakhulupirira mwa Iye. Kuweruza kwatsopano uku kuli ndi tanthauzo lanji?

Kwa zaka mazanamazana, Mulungu wakhala akuonetsera chikondi chake ndi kupereka chipulumutso kwa aliyense amene angachilandire.  Izi zapangitsanso choipa kuti chikhazikike momera mizu.



M'katikati mwa Chiweruzo, maiko onse ndi angelo okhulupirika awona chilungamo ndi chifundo cha Mulungu pothana ndi uchimo ndi mpanduko. Tsopano, iwo aona zotsatira zeni zeni za ulamuliro wausatana: dziko lopanda kanthu ndi labwinja.


Koma ife amene takhala mu dziko la m'dani pa nthawi ya mkanganowo, omwe taomboledwa tsopano, tidzafunikanso kuona chilungamo ndi chifundo cha Mulungu. Mu chiweruzo cha zaka chikwi tidzakhala otsimikizika kwathunthu za chikondi cha Mulungu kotero kuti choipa sichidzaukanso (Nahemiya 1:9).

# NTHAWI YA MOYO NDI IMFA

"Pakuti taonani, likudza tsiku, lotentha ngati ng'anjo; ndipo onse akudzikuza ndi onse akuchita choipa. Adzakhala ngati chiputu; ndi tsiku lilinkudza lidzawayatsa, ati Yehova wa makamu, osawasiyira muzu kapena nthambi" (Malaki 4:1)

"Koma inu akuopa dzina langa, dzuwa la chilungamo lidzakutulukirani, muli kuchiritsa m'mapiko mwake; ndipo mudzatuluka ndi kutumphatumpha ngati anaang'ombe onenepa otuluka m'khola" (Malaki 4:2)

Pamapeto a zaka chikwi, oipa adzaukitsidwa. Iwo akuvomeranso chitsogozo cha Satana, amenyananso ndi Mulungu komanso oyera mtima. Palibe chomwe chasintha, ndipo onse adzawonongedwa ndi moto (Chivumbulutso 20:5-9).



Koma asanawonongedwe, mlandu womaliza ukuweluzidwa. Mabuku atsegulidwa. Ndipo aliyense akuzindikira m'zolembedwa m'mabukumo zintchito zawo ndi kukanitsitsa kwawo maitanidwe achikondi a Mzimu Woyera. Onse adzavomereza chilungamo cha Mulungu, namugwadira Iye (Chivumbulutso 20:11-13; Yesaya 45:23; Afilipi 2:10).



M'malo mokhala ndi moyo wosatha (alangidwe kosatha), akuvutika ndi "imfa yachiŵiri," imene kulibe chiukiritso.(Chivumbulutso. 20:14-15; Masalimo 37:20; Malaki 4:1; Yesaya 26: 14).

Imfa ndi uchimo zatha. Ndi nthawi yopukuta misozi yonse ndi kusangalala ndi moyo wosatha komanso wachimwemwe (Chivumbulutso 21:4).



# NTHAWI YOKONDA NDI KUKONDEDWA


"Yehova anaonekera kwa ine kale, ndi kuti, Inde, ndakukonda iwe ndi chikondi chosatha; chifukwa chake ndakukoka iwe ndi kukukomera mtima" (Yeremiya 31:3)

**Tidzachita chiyani kwa muyaya mu dziko lapansi latsopano?**

- Mtanda wa Khristu udzakhala sayansi ndi nyimbo ya owomboledwa kwa muyaya.
- Pazigwa zamtendere, m'mphepete [...] mwa mitsinje yamoyo, anthu a Mulungu [...] adzapeza pokhala
- Kumeneko anzeru amuyaya adzalingalira mokondwera kosatha zodabwitsa za mphamvu ya kulenga
- Mphamvu iliyonse idzakulitsidwa, mphamvu iliyonse idzawonjezeka
- Kupeza chidziwitso sikudzakhala kotopetsa luntha kapena kutha mphamvu
- Zochita zazikuluzikulu zidzachitidwa, zokhumba zapamwamba kwambiri zidzakwaniritsidwa.
- Zochitika zapamwamba zidzabuka kuti zigonjetsedwe, zodabwitsa zatsopano zomwe zingasiririidwe, choonadi chatsopano kuti chimvetsetsedwe, zolinga zatsopano zomwe zokonzanso mphamvu za mzimu, moyo ndi thupi.
- Adzagawana [ndi zolengedwa zosachimwa] chuma cha chidziwitso chopezeka kwa zaka mazana pa malingaliro a ntchito za Mulungu
- Ndi masomphenya wooneka bwino, adzalingalira ulemerero wa Chilengedwe: dzuwa, nyenyezi ndi dongosolo lopatsidwa kwa izo, zungulira Mpando wa Umulungu







Extracted from "The Great Controversy", pp. 651, 666, 668, 675, 677, 678)

“Mkangano waukulu watha. Uchimo ndi ochimwa kulibenso. Chilengedwe chonse chiri changwiro. kugunda ngati kwa mtima umodzi, kwachiyanjano ndi chisangalalo kwafalikira mu chilengedwe chonse. Kuchokera kwa Iye amene adalenga zonse, moyo, kuwala ndi chisangalalo, kudutsa malo opanda malire. Kuyambira pa cholengedwa chochepesetsa, kufikira ku dziko lokulisitsa, zones, zamoyo ndi zopanda moyo, zinthu zones, mu kukongola kwawo kosaphimbika ndi Mthunzi, ndi chisangalalo changwiro, zimalengeza kuti Mulungu ndiye chikondi.”



EGW (The Great Controversy, pg. 678)